


# INE NDIKUDZIWA

 Ife ndithudi ndi anthu amwayi kukhala pano mmawa uno, kukhala amoyo pa dziko lapansi, kuwona nthawi ina yopambana ya Isitara. Isitara nthawizonse imabweretsa a—chinthu chaulemerero kwa ife, ziyembekezo zatsopano. Ndipo—ndipo ndi zopambana bwanji!

<sup>2</sup> Ndipo basi pamene ine ndimalowa mchipinda kumbuyo uko mmawa uno, winawake anakumana nane ndipo anati, “M’bale Branham, inu mukudziwa a—khanda, kapena mwana wamng’ono kapena winawake, anapemphereredwa ku Chautauqua chaka chatha, amene ankayenera kuti achotsedwe mtima wake, ndipo mavavu kapena chinachake kuti chikonzedwe pa iwo.” Anati, “Mwanayo anachiritsidwa, ndipo ali mchipinda mmawa uno, ndithudi, ndipo wakhala pano mmawa uno.” Chotero izo ziri bwino, ife tikhala ndi umboni waung’ono kuchokera kwa iye mwinamwake tisanalowe mu msonkhano winawo. Ndipo ndife anthu okondwa basi.

<sup>3</sup> Tsopano ine ndimufunsa M’bale Neville ngati iye angawerenge Lemba la Mateyu kapena Luka, limodzi, la chiukitsiro, ngati inu simunawerenge kale ilo. Inu mwatero, m’bale? [M’bale Neville akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Chotero, pamene ife tikukonzekera pemphero.

<sup>4</sup> Ndipo tsopano kutsatira msonkhano uno, ukhala msonkhano wa machiritso. Msonkhano uno ukatha, kenako inu mupita ku kadzutsa wanu. Kenako, zikatha zimenezo, ife tidzabwereranso pa hafu naini ndipo tidzayamba msonkhano wina. Ndipo kenako misonkhano ya machiritso idzatsatira umenewo. Ndipo kenako misonkhano ya ubatizo idzatsatira.

<sup>5</sup> Ndipo ndi nthawi yokongola bwanji ya ubatizo! Oh, mai! Chiukitsiro! Ndi chifukwa chake ife timabatizidwa, chifukwa chakuti Iye anaukanso.

<sup>6</sup> Ine ndikukumbukira ife tisanakhale ndi mobatizira mwathu pano, ine ndinkakonda kuwatengera iwo uko ku mtsinje kumusi kuno, molawira, mmawa wozizira ngati chisanu, ndi kukawabatiza anthu kumusi kumeneko pa mtsinje. Pali chinachake cha izo chimene, basi, iyo ndi nthawi yopatulika. Isitara, ndi nthawi yopambana.

Ine ndimamuyang’ana M’bale Pat Tyler wakhala apa.

<sup>7</sup> Ine ndimangoyankhulana ndi winawake usiku wapitawu. Kuti, msonkhano wathu womaliza mu Oklahoma, ine ndinayesera kuti, ndikuyesera tsopano (ndipo ine ndilengeza ichi) kuti ndisiye pambali kufikira Mulungu atandiitana ine kuti ndichite izo, utumiki wanga wakale wa kuzindikira za

mumtima, chifukwa ine ndikuganiza (poyambirira) ndi u—utumiki watsopano ukubwera.

<sup>8</sup> Usiku wina, aliyense asakudziwa kalikonse za izo, ine ndinayesera izo pa mwana akubwera pa nsanja, anali atabadwa wakhungu, khanda; ndipo anali wakhungu kwathunthu, mnyamata wa pafupifupi usinkhu wa zaka sikisitini. Ndipo nthawi yomweyo iye anafuula, “M’bale Branham, ine ndikukhoza kuwona!” Ndipo pamenepo, ndipo Pat anali... Ty-...atama pafupi, pafupi ndi mnyamatayo, pamene maso ake anatseguka koyamba mmoyo wake wonse. Ndipo chotero ine ndikudalira kuti inu pano, ndi chiyembekezo chachikulu, ndi inemwini, ine ndikuyembekeza chinachake, Mulungu kuti atichitire ife, ndi kutibweretsa ife pa mulingu wina kuposa umene ife takhalapo.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano ku pemphero.

<sup>9</sup> Atate athu Akumwamba Achisomo, pamene ife tasonkhano mmawa uno, pano mu tchalitchi chaching’ono mmphepete mwa msewu, ife tiri othokoza ndithudi kwa Inu, chifukwa cha chimene zonsezi zikutanthauza kwa ife, ndipo makamaka mmawa wa Isitara uno. Ngati pakanati pasakhale Isitara, ife sibwenzi tiri mu chikhaliidwe chimene ife tirimo lero. Kutu, Isitara ndi imene inasindikiza malonjezo onse a Mulungu. Iyo inatsimikizira iwo kwa ife. Chirichonse chimene Iye anayamba wachilonjezapo, izo zonse zinapangidwa kukhala zenizeni pa Isitara. Limodzi la masiku opambana a chikondwerero amene ife tingakhale nalo mu chaka! Ndipo ife tikufuna kupempha, Ambuye, lero, kuti Inu mutonthoze mitima yathu pamene ife takhala, tikudikirira, ndipo tiri pansu pa kuyembekezero Mzimu Woyera, Umene unabwera itachitika Isitara, kuti ubwere pa mitima yathu ndi kudzatitonthoza ife, ndi kudzabwezeretsa chikhulupiro chatu, mwa muyezo waukulu wamphamvu, kuti ife tikakhoze kuyenda moyo umene Yesu watizodzera ife kuti tiyendemo.

<sup>10</sup> Ife tikupempherera munthu wina aliyense, ndipo makamaka iwo amene atsekeredwa mkati ndipo akulephera kuti abwere ku misonkhano kulikonse lero. Mulungu, mukhale nawo iwo. Ndipo mulole—mulole Isitara iyi iwapezere iwo Isitara yeniyeni, kudzuka kuchoka pa bedi, ndi thanzi latsopano limene iwo sanalidziwepo nkomwe mmoyo mwawo. Perekani izi, Ambuye.

<sup>11</sup> Mulole mlaliki aliyense, wantchito aliyense amene Inu muli naye kuzungulira dziko lero, amene akukondwerera chikumbutso chachikulu ichi, mulole iwo akhale ndi chisankho ndi nyonga ndi Mphamvu, kuti akabweretse kwa osonkhana awo (nkhosa yoyembekezero) Chakudya chimene Mulungu wawasungira anthu Ake. Perekani izi, Ambuye. Ife tikudikirira gawo lathu, modzichepetsa, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Amenii.

<sup>12</sup> Ine ndikufuna M'bale Neville tsopano kuti awerenge Malemba a chiukitsiro. [M'bale Neville akuti, "Mateyu 28," ndipo akuwerenga Malemba otsatirawa—Mkonzi].

[*Pakutha pa sabata, pamene kunayamba kucha kulowa mtsiku loyamba la sabata, kunabwera Mariya wa Magadala ndi Mariya winayo kuti adzawone manda.*]

[*Ndipo, taonani, panali chivomezi chachikulu: pakuti mngelo wa Ambuye anatsika kuchokera kumwamba, ndipo anabwera ndipo anadzawugudubuzwa mwala kuwuchotsa pakhomo, ndipo anakhala pa iwo.*]

[*Nkhope yake inali ngati mphenzi, ndipo chovala chake ngati chipale.*]

[*Ndipo pomuwopa iye oyang'anirawo ananjenjemera, ndipo anakhala ngati anthu akufa.*]

[*Ndipo mngelo anayankha ndipo anati kwa akaziwo, Musawope ayi: pakuti ine ndikudziwa kuti inu mukumufuna Yesu, amene anapachikidwa.*]

[*Iye sali pano: pakuti iye wauka, monga iye ananenera. Bwerani, mudzawone malo amene Ambuye anagona.*]

[*Ndipo pitani mwamsanga, ndipo mukawauze ophunzira ake kuti iye wauka kwa akufa; ndipo, taonani, iye akupita patsogolo panu kulowa mu Galileya; kumeneko inu mukamuwona iye: taonani, ine ndakuuzani inu.*]

[*Ndipo iwo ananyamuka mwachangu kuchoka kumanda ndi mantha ndi chimwemwe chachikulu; ndipo anathamanga kuti akawauze ophunzira ake.*]

[*Ndipo pamene iwo anapita kukawauza ophunzira ake, taonani, Yesu anakumana nawo, anati, Nonse taonani. Ndipo iwo anabwera ndipo anagwira mapazi ake, ndipo anampembedza iye.*]

[*Kenako Yesu anati kwa iwo, Musawope: pitani mukawauze abale anga kuti apite ku Galileya, ndipo kumeneko iwo akandiwona ine.*]

[*Tsopano pamene iwo ankapita, taonani, oyang'anira ena anabwera mu mzinda, ndipo anawonetsera kwa ansembe aakulu zinthu zonse zimene zinachitika.*]

[*Ndipo pamene iwo anasonkhana ndi akuluakulu, ndipo anakambirana, iwo anapereka ndalama zochuluka kwa asirikari,*]

[*Akuti, Mudzanene inu, ophunzira Ake anabwera usiku, ndipo anadzamuba iye pamene iwo amagona.*]

[*Ndipo ngati izi zifika mmakutu a kazembe, ife timukopa iye, ndi kumutetezera iye.*]

[Chotero iwo anatenga ndalama, ndipo anachita mmene anawauzira: ndipo maneno awa amanenedwa mwawamba pakati pa Ayuda mpaka lero.]

[Kenako ophunzira leveni anapita ku Galileya, ku phiri limene Yesu anawasankhira iwo.]

[Ndipo pamene iwo anamuwona iye, iwo anampembedza iye: koma ena anakaikira.]

[Ndipo Yesu anabwera ndipo anayankhula kwa iwo, anati, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa ine kumwamba ndi padziko lapansi.]

[Chotero inu mupite, ndipo mukaphunzitse mafuko onse, kuwabatiza iwo mu dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:]

[Kuwaphunzitsa iwo kuti azichita zinthu zonsezi zimene ine ndakulamulani inu: ndipo, taonani, ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka kumathero a dziko lapansi. Amen. Malo osajambulidwa pa tepi.]

<sup>13</sup> . . .awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake.

<sup>14</sup> Tsopano tikufuna kunena, kulengezanso tsopano, kuti misonkhano, ndipo ya mmawa, ipitirirabe pa hafu-naini, mwamsanga tikachoka ku uwu, a . . .msonkhano wa mmawa uwu tsopano. Ndiyeno ife tikuwutcha uwu msonkhano wathu wa kutuluka kwa dzuwa. Ndipo ife tiri, tiri ndi zinthu zina zazikulu zoti tilengeze kwa inu zokhudza a—misonkhano imene yadutsa. Ndipo tikufuna inu amene mukudwala ndi osautsika, nonse a inu, kuti mubwere ndi chikhulupiriro mmawa uno, kudzakhulupirira kuti Yesu wowukitsidwa uyu ali moyo lero, ndipo Iye ali yemweyo basi monga Iye amakhaliwa nthawizonse. Iye sanasinthe mpang’ono pomwe.

<sup>15</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge gawo laling’ono la Lemba apa, lopezeka mu mutu wa 19 wa Yobu, kuyambira ndi ndime ya 15.

*Iwo amene akukhala mnyumba yanga, . . . adzakazi anga, akundiwona ine ngati mlendo: ine ndi mlendo pamaso pawo.*

*Ine ndinamuitana wantchito wanga, ndipo iye sanati andiyankhe ine; ine ndinamuchondelera iye ndi kamwa langa.*

*Mpweya wanga ndi wachirendo kwa mkazi wanga, ngakhale ine ndinamuchondelera chifukwa cha ana a mnofu wanga womwe.*

*Eya, ana anandinyoza ine; ine ndinauka, ndipo iwo anayankhula monditsutsa ine.*

*Azimzanga onse amkati akundida ine: ndipo iwo amene ine ndinawakonda akunditsutsa ine.*

*Mafupa anga alekana ndi khungu langa ndi mnofu wanga, ndipo ine ndatsala ndi khungu la mano anga.*

*Chitirani chifundo pa ine, chitirani chifundo pa ine, O inu amzanga; pakuti dzanja la Mulungu landikhudza ine.*

*Nchifukwa chiyani inu mukundizunza ine ngati Mulungu, ndipo simukukhutitsidwa ndi mnofu wanga?*

*Oh kuti mawu anga tsopano analembedwa! oh kuti iwo analembedwa mu bukhu!*

*Kuti iwo anazokotedwa ndi cholemba cha chitsulo ndi kuyikidwa mu thanthwe kwa nthawizonse.*

*Pakuti ine ndikudziwa . . . muomboli wanga ali moyo, ndipo kuti iye adzaima pa tsiku lotsiriza pa dziko lapansi:*

*Ndipo ngakhale patatha . . . mphutsi za khungu zitawononga thupi ili, komabe mu thupi langa ine ndidzamuwona Mulungu:*

*Amene ine ndidzamuwone inemwini, . . . maso anga adzamuwona, ndipo osati wina; ngakhale impsyo yanga itadyeka mkati mwanga.*

<sup>16</sup> Ine ndikufuna kuti nditenge kwa phunziro pamenepo, lopezeka mu Yobu 19 uyu. *Ine Ndikudziwa.*

<sup>17</sup> Mbadwa pa nthawi iyi inali mwanjira yina monga ife tiriri lero. Iye anali mmavuto aakulu, monga ife timanenera izo, “mmadzi akuya,” ndipo iye anali wosimidwa. Masiku ambiri iye amakhala pa mulu wa phulusa, ndipo amayesera kuti apeze mawu oti amutonhoze iye, kuyesetsa kuti apeze chinachake chimene chingamulimbikitse iye, ndi chinachake chimene chingati—chingakhale chitonhozo kwa iye pamene iye amawuwona moyo wake ukumuchokera iye.

<sup>18</sup> Poyambirira, iye anali bambo wokalamba, mwinamwake usinkhu wa zaka nainte, ndipo anali atakanthidwa ndi dzanja la Mulungu. Tsopano, ife tikudziwa kuti Mulungu sanamukhudze iye ndi dzanja Lake, koma kuti Mulungu anamulola Satana kuti amukhudze iye. Mulungu amangokhala ndi antchito oti achite zinthu. Mulungu akafuna choipa chichitidwe, Iye amangomumasula Satana kuti akachite icho. Ndipo ngati Iye afuna chabwino chichitike, Iye ali ndi antchito Ake amene amawamasula kuti akachichite icho.

<sup>19</sup> Ndipo Satana anali atamugwira Yobu ndi cholinga, kuti amuyese iye, chifukwa iye ndi Mulungu anali ndi mtsutsano. Ndipo Mulungu anamuza Satana kuti, “Ine ndiri naye wantchito pa dziko lapansi, palibe aliyense wofanana ndi iyeyo.

Chirichonse chimene Ine ndinganene kwa iye, iye amakachita icho. Iye ndi munthu wangwiro, ndiponso munthu wolungama.”

<sup>20</sup> Ndipo Satana anati, “Ngati Inu mutangondilola ine ndimutenge iye, ine ndingamupangitse iye kuti akunyozeni Inu pa nkhope Yanu.”

<sup>21</sup> Yobu, osadziwa kuti zinthu zonsezi zimachitika, izo zinamuyika mbadwayo mu kupsyinjika kwakuya. Komabe, mwanjira ina, pamene zonse zinamuchokera iye, iye anawasungabe malo ake mwa—mwa Khristu. “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo,” iye anatero.

<sup>22</sup> Tsopano ife timabwera ku malo amenewo. Ife tonse timabwera. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti lero, kuti ife tasonkhana pano chifukwa cha chinachake chonga cholinga chomwecho. Ife tonse tiri pa mulu wa phulusa. Ife tiri ndi mavuto athu, ndi zokwera ndi zotsika zathu, ndi zathu—nthawi zathu zovuta, ndi matenda athu, ndi kupweteka kwa mtima kwathu, ndi zokhumudwitsa zathu. Chotero ife tikubwera chomwechi, mmawa, mmawa wa Isitara uwu, kuti tidzapeze mawu achitonthozo, monga Yobu anali kuyesetsa kuti awapeze kuchokera kwa azimzake.

<sup>23</sup> Palibe aliyense wa iwo amene akanamupatsa iye chitonthozo chirichonse. Chifukwa cha vuto lake, iwo anali kumunena iye kuti anali wochimwa wa mseri. Kenako, mkati mwa vuto lonselo, Mulungu anabwera kudzamupulumutsa iye.

<sup>24</sup> Yobu anali kufunsa. Monga mmene iye amadziwira, sikuti nthenda yake yokha ndi zithupsya zake, ndi mavuto ndi kupweteka kwa mtima, chifukwa chotaya banja lake ndi chuma chake chonse, zinangotsala pang’ono kuti zitenge moyo wake; koma iye anali bambo wokalamba, wokanthidwa mu zaka, ndipo amadziwa kuti anali akupita ku manda. Ndipo, akudziwa zimenezo, iye amakhulupirira kuti panali winawake amene anamubweretsa iye pa dziko lapansi, iye sakanangobwera kuno payekha. Ndipo iye ankadziwa kuti anachokera kwa abambo ndi amayi, koma, komabe, abambo amenewo ndi amayi ankayenera kukhala ndi winawake woti awabweretse iwo. Ndipo izo zimangobwerera kuchiyambi, “Ndani anamubweretsa woyambayo, mmodzi?”

<sup>25</sup> Ndiyeno iye amadabwa izi. “Ndi chinthu chachirendo kuti ndiri pano, ndikuyendayenda, moyo wapamwamba kuposa wazinyamawo, ndi moyo wapamwamba kuposa moyo wa zomera.” Komabe ife tikupeza kuti iye anati, “Ngati mtengo ukafa, iwo umakhalanso moyo. Ndipo ngati a—duwa likafa, ilo limakhalanso moyo.” Koma iye anati, “Munthu akagona mnthaka, iye amapereka mzimu wake, ndipo iye amakhala alikuti? Ana ake amabwera kudzamulira iye ndi kudzachita ulemu, ndipo iye sazindikira izo ayi.” Ndipo iye anali kudabwa, “Vuto ndi chiyani kuti—kuti Mulungu akhoza kulola moyo

ngati umenewo kukhalanso moyo kenanso, monga ngati maluwa ndi zomera, koma munthu osakhalanso moyo?” Zonsezi zinali kumusautsa iye.

<sup>26</sup> Ndipo ngati ife tingatenge kuchokera pa kugamula uku mmawa uno. Ndipo ndicho chimene ife tadzera pano. Ife tamva nkhani ya Isitara, mobwereza ndi mobwereza, ndipo taiwerenga iyo mobwereza bwereza; ndipo lero, pa zolengeza zanu za pa walesi, inu mumva atumiki osiyanasiyana akukamba zimenezo. Koma chimene ine ndimaganiza, kwa gulu langa laling’ono mmawa uno, limene Ambuye andipatsa ine, ine ndizifikira izo kuchokera pa maimidwe osiyana ngati ine ndingathe, kubwera pa malo a: Nchifukwa chiyani ife timabwera ku mavuto amenewa? Nchiyani chimapangitsa zinthu zimenezi kuti zibwere? Nchifukwa chiyani Mkhristu kuti azisautsika konse? Nchifukwa chiyani kuti chirichonse, sichikumangoyenda mwangwiro kwa Mkhristu? Koma izo sizitero, ndipo ife tikudziwa zimenezo.

<sup>27</sup> Ndipo nthawizina ife timakhala ndi mavuto ochuluka pamene ife tikhala Mkhristu kuposa pamene ife tinali ochimwa. Chifukwa, Kunalembedwa, “Zochuluka ndi zosautsa za orungama, koma Mulungu amawawombola iwo kwa zonsezo.” Mulungu analonjeza masautso ochuluka, zomverera zachirendo, ndi zinthu zachirendo zimene zidzakhale zodutsa kuganiza kwathu, koma nthawizonse izo zimachitika kwa ubwino wathu. Ife timalephera basi kuzimvetisa izo, chifukwa, ngati tikanamatero, ndiye sibwenzi chiri chikhulupiriro kwa ife; ife bwenzi tikumayenda ndi kumvetisa. Koma ife timachita izo, ndipo tiri nazo izo, ndipo ife timakhulupirira mwa chikhulupiriro, Mawu Ake, kuti izo zidzachita chinthu china chabwino kwa ife. Ngati ife tingazimvetse izo lero, mwa chonchi—mmawa uno. Ngati ife tingamvetse kuti mavuto athu onse. . . Ndipo palibe aliyense wa ife amene ali woti izo sizingamuchitikire. Ndipo ngati ife tingazindikire kuti zinthu zimenezo ndi za kwa ubwino wathu!

<sup>28</sup> Kunalembedwa, mu limodzi la Malemba mu Baibulo, kuti, “Mayesero amene amabweretsedwa pa ife, ndi ofunikira kwambiri kwa ife kuposa golide, pakuti ndi Mulungu yemwe amatipatsa ife mayesero amenewa.” Ife titatha kukhala anthu Ake, kuvomereza kwathu ndi ubatizo wathu, ndi lonjezo lathu kuti tiziyenda mmoyo chifukwa cha Iye, ndiye yesero lililonse limene limabwera pa ife ndi loti litipange ife kukhala angwiro kwa ulemelero Wake. Ilo ndi lakuti litibweretse ife pa malo amene Mulungu akhoza kudzipanga Yekha weniweni kwa ife kuposa mmene Iye analiri yesero lisanabwere.

<sup>29</sup> Ine ndikufuna kuti ndilumikizane mmawa uno ndi Yobu, kunena kuti ndakhala nthawi yaitali kuti ndidziwe kuti icho ndi Choonadi. Ine ndaziwona izo mmoyo wanga womwe, kuti nthawi iliyonse chochitika chachikulu chikabwera,

chimene ine sindingachizungulire, kapena kupita pansu pake kapena pamwamba pake, Mulungu amakonza njira, ndipo ndimatulukamo mwaulemelo. Ine ndikungodabwa mmene chisomo Chake nthawizonse chimachitira izo, koma Iye amachita izo.

<sup>30</sup> Ndipo kumbukirani, mu zinthu zonsezi, Satana amayesetsa kuti atipangitse ife tikhale amanjenje, ndi kumatibalalitsa ife, kuti atipangitse ife kumaganiza, “Oh, nchifukwa chiyani *izi* zinachitika? Nchifukwa chiyani ine sindinakhale monga *ichi*?”

<sup>31</sup> Masiku pang’ono apitawo pamene ine ndinatuluka ku malo okongola kwambiri, ndi owoneka bwino kwambiri amene ine ndinayamba ndawawonapo mmoyo wanga wonse, iyo inali nyumba yaikulu ya m’bale wathu, Oral Roberts. Pamene ine ndinawona nsangalabwi wolimba uwo, ndipo yopanda zenera pa iyo, koma mmene iyo inakonzedwera! Ndipo ine ndafikako ku Hollywood ndipo ine ndakhalapo mu nyumba zachifumu, ndipo ine ndakhalapo kulikonse kumene ine ndingakhale, ndithudi, kuzungulira dziko, ndi zokongola zonse, malo okondeka ndi nyumba, koma ine sindinawonapo chirichonse, malo aliwonse, oti ndingawafanizitse, ndi iyo, kulibe kulikonseko. Mmene mawaya a aluminiyamu aang’ono amalukanirana—mkati limodzi, ndipo, oh, ine sindinawonapo chirichonse chokongola chomwecho mmoyo wanga wonse. Pamene ine ndinayenda kudutsa pamenepo, ndikutenga manja anga ndi kusisita zipupa zimenezo, ndi—ndi nsangalabwi wapamwamba; zonse mmaonekedwe a utatu wa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, zo—zosema za izo. Zinthu zonsezo! Ine ndinali nditangobwera kuchokera kwa M’bale Tommy Osborn, ndipo nditawona ntchito yake yaikulu, yamphamvu kumeneko ya Ambuye.

<sup>32</sup> Ine ndinaima panja, ndinayang’ananso pa nyumbayo, ndipo ine ndinaganiza, “Mulungu, ndithudi ine ndasanduka wachinyengo, ndithudi ine ndasanduka wotayika, penapake; pakuti, mautumiki a amuna awa anachokera kwa wanga.” Ndipo ine ndinaganiza, “Nchiyani? Mwinamwake ndine wosadalirika kwambiri, Ambuye, kuti Inu simungathe kundidalira ine ndi chirichonse chonga zimenezo. Ngakhale timadolla, tapang’ono timene Inu mumandilola ine kuti ndilipirire misonkhano ndi zinthu, tsopano iwo akuyesetsa kuti anditumize ine ku ndende chifukwa cha ito. Ndipo nchifukwa chiyani ine ndiri wachinyengo chomwecho, kapena nchifukwa chiyani ine ndiri munthu wosadalirika chomwecho?”

Ine ndinali pa mulu wa phulusa, monga Yobu wakale.

<sup>33</sup> Pamene ndinadzaima panja kumeneko, kulephera ngakhale kuti ndipume, chifukwa cha ulemelo umenewo; kuti mnyamata wosauka wobadwira mu dzenje, wachi Pentekoste, angachite ndi



kuipanga iyo kukhala nyumba yaikulu yapamwamba. Ndipo ine ndinaganiza, “O Mulungu, mwinamwake sindine woyenera.”

<sup>34</sup> Basi pomwepo Liwu laling’ono linadzatsika kudutsa mtinjira timeneto, ndipo linati, “Koma Ine ndi gawo lako.”

<sup>35</sup> Kenako ine ndinaganiza, “O Ambuye Mulungu, oh, mungolola kuti izo zikhale mwanjira imeneyo, ndiye, Ambuye. Ine. . . chifukwa ine sindingakhale ndi luntha lochitira ntchito yayikulu ngati imeneyo kwa Inu. Ndipo ine ndi—munthu wosaphunzira. Koma, bola ngati Inu muli gawo langa, ine ndi Wanu, ndipo Inu munditsogolera ine. Ine sindingathe kudzitsogolera ndekha. Koma, O Ambuye, nditsogolereni ine!”

<sup>36</sup> Ndi maora ovuta amenewo amene amatifinyira ife pa mchenga wopatulika umenewo. Izo zinali mu Baibulo. Ndipo kumbukirani, ziribe kanthu mmene kupsyinjikako kuliri kwakukuru, Satana sangathe kuwuchotsa moyo wanu kufikira Mulungu atathana nanu inu. Palibe chirichonse chimene chingachitike kwa inu pokhapokha Mulungu atachiloleza icho. Palibe choipa chimene chingabwere pokhapokha Mulungu atachiloleza icho. Ndipo izo ndi za kwa ubwino wanu kuti Iye akuchita zimenezo. Tatiyeni tiganize.

<sup>37</sup> Kumeneko pamene chigumula chinabwera kudzawononga dziko, icho sichikanatha kumuwononga Nowa. Nowa sakanawonongedwa, chifukwa chakuti Mulungu anali ndi ntchito yoti iye ayichite.

<sup>38</sup> Tsiku lina, kumusi mu fuko lalikulu liri pansu pa ukapolo waukulu, kunali ana ena Achihebri amene ife timawadziwa ngati Shadreki ndi Misheki ndi Abednego. Ndipo zinafika pamalo amene iwo ankayenera kuti apange chiganizo, kuti chinachake chinkayenera kuti chichitike. Iwo anali. . . Chawo—chawo—chikhulupiriro chawo chinayikidwa pamayesero.

<sup>39</sup> Ndipo pamene chikhulupiriro chako chiyikidwa pamayesero, ndiye usalephere. Ukhalebe ndi chimene iwe ukuchikhulupirira.

<sup>40</sup> Ndipo pamene chikhulupiriro chawo chinayikidwa pamayesero. Ndipo iwo anapita ku ora lovutalo. Sikuti iwo anangopita ku—ku mulu wa phulusa, koma iwo analowa mu ng’anjo ya moto. Koma Satana sakanatha kuti awawononge iwo, pakuti cholinga cha Mulungu chinali chisanakwaniritsidwebe. Iwo amalowa mmenemo ndi chiyembekezo ichi, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo!” Iwo amalowa mmenemo ndi chiyembekezo ichi apa, “Ife ndi otsimikiza kuti Mulungu ndi wokhoza kutipulumutsa ife ku ng’anjo ya moto iyi, koma, komabe, ife sitikagwadira chifanocho.”

<sup>41</sup> Satana sakanawatenga iwo. Iye sakanamumiza Nowa mu chigumulacho, kufikira cholinga cha Mulungu chitakwaniritsidwa. Iye sakanawawotcha ana Achihebriwo, kufikira cholinga cha Mulungu chitatsirizika. Iye sakanatha

kumupha Yobu ndi zithupsya ndi mavuto, kufikira cholinga cha Mulungu chitatsirizika. Komanso mikango sikanamudya Daniele, kufikira cholinga cha Mulungu chitatsirizika. Komanso imfa ndi ukalamba sizikanamutenga Abrahamu, mpaka cholinga cha Mulungu chitatsirizika.

<sup>42</sup> Ndipo iyo singakutengeni inu, kapena kunditenga ine, mpaka cholinga cha Mulungu, cha moyo wathu, chitatsirizika. Chotero, ife timapeza kuchokera pamenepo, chitonthozo.

<sup>43</sup> Ndipo nchifukwa chiyani Mulungu amaloleza kuti mavuto azibwera? Mulungu amawalera mavuto, amayika mano mkamwa mwake ndipo amapangitsa iwo kumumvera Iye, ndipo mavuto amenewo amatibweretsa ife mu chiyanjano chapafupi ndi Mulungu.

<sup>44</sup> Panali palibe utawaleza kufikira chigumula chitabwera. Koma Nowa ataikidwa mu chochitika chimenecho chimene iye analimo, kuti ayandame masiku forte ndi mausiku, mu namondwe, ndi chombo chaching'ono chikumenyetseka mmwamba ndi pansi mmadzi; izo zinali chigumula chitatha, mpamene iye anawona utawaleza kwa nthawi yoyamba, pangano la chiyembekezo, pangano la lonjezo. Iye atatha kudutsa mu chisautso, kenako iye anawona lonjezo.

<sup>45</sup> Umo ndi mmene iwe umawonera lonjezo, utatha kudutsa mu chisautso. Ine ndimaikonda ndakatulo ija, kapena salmo:

Kodi ndinyamulidwe kupita kwathu  
Kumwamba  
Pa kama wa maluwa wophweka,  
Pamene ena anamenyera kuti apeze mphotho  
Ndipo anayenda pa nyanja za magazi?

<sup>46</sup> Ife timapempha chitonthozo ndi mtendere. Mulungu amatipatsa ife chopambana chimene Iye akanatipatsa ife: mayesero ndi zisautso. Izo ndi zabwino kuposa chitonthozo ndi mtendere. Chitonthozo chatu chiri kutsidya kwa mtsinje.

<sup>47</sup> Izo zinali mpaka ana Achihebri atakakamizidwa kulowa mu ng'anjo ya moto, pa amodzi a mayesero awo opambana, kuti iwo anamuwona Mmodzi wofanana ndi Mwana wa Mulungu atayima pakati pawo. Mavuto awo anadzapereka Mwana wa Mulungu ndipo anaima pakati pawo, mu mphepo, kuti azikupizira kutenthako kutali. Koma osati kufikira atalowa mu moto mpamene Mtonthoziyo anawonekera.

<sup>48</sup> Anali Daniele amene analinga mu mtima mwake kuti iye sadzaziwononga yekha ndi zinthu za mdziko, ndipo anakakamizidwa kudutsa mu yesero, kusankha kuti iye apemphera kwa Mulungu kapena kuti apita ku dzenje la mikango. Koma zinali kuti pamene moto unayatsidwa, ndipo iye nkuponyeredwa mu dzenje la mikango, kuti, zitachitika zimenezo, mpamene iye anawona Mngelo wa Ambuye atayima pakati pa iye, akuingitsira kutali, Lawi la Moto lalikulu lija

litaima pakati pa iye ndi mikango. Ndipo mikangoyo imalephera kuti imugwire iye, chifukwa iye anali atadutsa mmayesero ndi mayeso ndi mavuto. Ndipo iye anadziwa kuti Mulungu wake anali wothekera kumupulumutsa iye ku zimenezo.

<sup>49</sup> Anali Abrahamu, iye atatha kuwona kuti nthaka ikuuma, ndipo chilala chabwera, ndipo Loti wadzilekanitsa yekha ndipo wapita uko kukakhala mosangalala mdziko. Izo zinachitika iye atamva kunyinyirika ndi kulira kwa—kwa olishya ziweto ake, ali opanda udzu wa ng’ombe zake, koma iye anakhalabe mu dziko limene Mulungu anamupatsa iye ndi kumuuzwa iye kuti adzakayendamo. Ndipo monga pa tsiku limenelo, iye atayesedwa mpaka chake—chipiriro chake chitafika pamapeto, linali tsiku limenelo limene, pamene mayesero anali atatha, iye anayankhulana maso ndi maso ndi Elohim pansu pa mthundu tsiku limenelo. Zinali atatha kuvutika ndi mayesero ake, iye atadutsa mmavuto amene iye anadutsamo, mpamene Mulungu anawonekera kwa iye mmawonekedwe a Munthu; ndipo anadzakhala pamenepo ndipo anamuuzwa iye kuti anali wokwatira ndipo dzina la mkazi wake linali Sarah, ndipo anati iye anamuseka Iye, ali mu hema kuseri. Panali pamenepo pamene Abrahamu anamutcha Iye “Elohimu.” Izo zinali pambuyo pa mayesero ndi chisautso.

<sup>50</sup> Oh, ngati Mpingo utangodzuka kwa Iwomwini lero, kuti uzindikire kuti atatha mavuto ndi mayesero, ndi kusekedwa ndi kunyozedwa, zinthu zimene Mpingo wadutsamo, Mpingo wa pentekoste; ndi pamene timamuwona Mulungu ali pakati pathu, akuchita zizindikiro zazikulu, ndi zodabwitsa.

Zikadzatha zothodwetsa ndi mavuto a tsikuli,  
Zonse zikadzatha,  
Ndiye ife tidzamuwona Yesu pamapeto.  
Iye adzakhala akundidikirira ine,  
Yesu wachilungamo ndi woona,  
Pa mpando wachifumu Wake wokongola,  
Iye adzatilandira ife Kwathu  
Tsiku likadzatha.

Kukadali kowala, tiyeni tigwire ntchito.

<sup>51</sup> Amuna opambana onse awa, amene angatenge zochuluka za msonkhano wathu wa mmawa uno, tikayamba kuwatchula iwo. Iwo anadutsa mmayesero, ndipo anamuwona Mulungu. Iwo anadutsa mmayesero, ndipo anawawona Angelo. Iwo anadutsa mmayesero; ndi mmavumbulutso, ndipo anawona zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi zinthu.

<sup>52</sup> Koma, oh, palibe aliyense wa iwo amene anawona zimene Yobu anaziwona. Amuna onsewo, atatha kuwawona Angelo, ndipo nkumuwona Mulungu ndi zinthu zonsezi, iwo sanawone konse kalikonse koti kawapatse iwo chiyembekezo kuseri kwa manda. Koma Yobu anawona chiwukitsiro! Iye anawona Isitara.

Iye anawona chinthu chimene chimatonthoza mtima uliwonse. Ndiye pamene iye anatero, “O ngati mawu anga angalembedwe mu bukhu! O ngati iwo angazokotedwe ndi cholembere cha chitsulo, pa thanthwe!”

<sup>53</sup> Atawona, izo, chirichonse chinali chitamuwukira iye. Ake, ngakhale antchito ake samamuyankhulitsa iye nkomwe. Mkazi wake anali mlendo. Anakhala pamenepo, pa mulu wa phulusa, yesero lalikulu lija. Ndipo mpingo unabwera, ndipo unatembuzira nsana wake kwa iye, kwa masiku seveni. Ndipo panalibe aliyense woti amutonhoze iye!

<sup>54</sup> Kenako iye ayenera kuti anawona masomphenya a Isitara, pamene iye anafuula, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo, ndipo mmasiku otsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi. Ine ndikudziwa! O ngati mawu anga angalembedwe ndi cholembere cha chitsulo, pa mwala, ngati mawu anga sangazilarenso, pakuti ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo! Ine ndikudziwa! Ine ndikudziwa!”

<sup>55</sup> Iwe ukudziwa chiyani, Yobu? “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo.” Kodi inu munazindikira, apo sipanangokhala Winawake alimoyo, koma Iye anali Muomboli kwa Yobu!

<sup>56</sup> Oh, lodala likhale Dzina la Ambuye. Ndine wokondwa kwambiri kuti ndine gawo la Isitara, kuti ndine gawo la chiukitsiro chimenecho! Ndipo ife ndi gawo la izo mmawa uno, chifukwa mwa ife mukukhala Moyo wa chiukitsiro uja (ndiwo, olandira nawo) umene unabweretsa Isitara. “Ine ndikudziwa kuti Muomboli wanga. . .” Iwe ukudziwa chiyani? Ine sindikungopeka izo; zachuluka zongopeka lero. “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo!” Inde, bwana.

<sup>57</sup> Tsopano kodi Iye anali chiyani? Ngati Iye anali moyo, Iye anali Muomboli kwa Yobu. “Wanga,” wake wake, *wanga*, “Muomboli wanga ali moyo!”

<sup>58</sup> Ndipo ndi chiyandinso chimene iwe ukuchidziwa, Yobu? Iwe unawona chiyani mu masomphenya amenewo? “Ndipo mmasiku otsiriza, Iye adzayima pa dziko lapansi. Ndipo ngakhale mphutsi za mkhungu zitawononga thupi langa, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu, Amene ine ndidzamuwona ndekha. Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo, ndipo Iye adzaima pa tsiku lotsiriza pa dziko lapansi. Ngakhale impyzo zanga zitadyedwa mkati mwanga, ngakhale mphutsi za mkhungu zitawononga thupi langa, komabe mthupi langa ine ndidzamuwona Mulungu.” Kudzera pamenepo panali masomphenya aakulu kwambiri.

<sup>59</sup> Daniele anamuwona Mngelo. Ana Achihebri anamuwona Mwana wa Mulungu. Nowa anawona utawaleza. Abrahamu anamuwona Mulungu, maso ndi maso. Koma, Yobu anawona chiukitsiro, Yobu anayang’ana mtsogolo. Mbadwa zonse ndi oyoera opambana, a mu Baibulo, anali kuyang’ana mtsogolo ku

tsiku limenero; ali ndi chitsimikizo, kudzera mu masomphenya awo, kudzera mu mavumbulutso awo, kuti kudzabwera nthawi ya chiukitsiro.

<sup>60</sup> Tsopano ife timawona ntchito zazikulu zikuchitika. Ife timawona mphamvu zazikulu za Mulungu. Ife timawona zinthu zazikulu zimene Iye angathe kuchita. Iwe sungayang'ane pa dzuwa ndi—ndi kudziwa kuti si Mphamvu ya Mulungu imene imapangitsa dziko kumazungulira pa dzuwa limenelo. Iwe sungawone nthawi ya dzinja ikubwera wopanda kudziwa kuti Mulungu alipo. Iwe ukhoza kuwona kuchiritsidwa kwa maso akhungu, makutu ogontha, nkudziwa kuti ndi Mulungu. Koma nanga bwanji ngati izo zitakhala zonse zimene ziripo, ndipo ife tikatha kufa basi zathera pomwepo? Koma chiukitsiro, Isitara, oh, ndi chimene chinasindikiza chirichonse chimene Mulungu analonjeza, chinali chiukitsiro.

<sup>61</sup> Ndipo iwo akuyenera kukhala ndi kupachikidwa, inu musanakhale ndi chiukitsiro. Ndipo Mpingo usanathe konse kuwona Mphamvu yowukitsidwa, ine ndisanawone konse utumiki watsopano ukuchitika inemwini, inu musanalowe konse mu chiyanjano chatsopano ndi Mulungu, pakuyenera kukhala kupachikidwa kwa wekha ndi cholinga chakuti padzabwere chiukitsiro. Ife tikuyenera kufa kwa malingaliro athu omwe, kufa kwa njira zathu zomwe, kufa kwa chirichonse chimene chatizungulira ife, kudutsa mmayesero ndi mmasautso, kuti ife tikathe kuwona chiukitsiro chatsopano, Moyo watsopano. Wochimwa asanakhale konse Mkhristu, pakuyenera kubwera imfa, kenako chiukitsiro.

<sup>62</sup> Abrahamu asanamuwone Elohimu, pankayenera kukhala zaka twente-faifi za kuyesedwa. Ana a Chihebri asanamuwone Mwana wa Mulungu, iwo ankayenera kukalowa mu ng'anjo ya moto. Daniele asanamuwone Mngelo, ankayenera kukalowa mu dzenje la mikango. Yobu asanachiwone konse chiukitsiro, iye ankayenera kuti alowemo ndi kutaya chirichonse chimene iye anali nacho; koma kenako, mwa masomphenya, iye anawona!

<sup>63</sup> Ndipo ngati Yobu mwa masomphenya anaima mokhazikika pa lonjezo, ife tikuyenera kuchita mochuluka bwanji, Khristu atatha kuwuka kwa akufa ndipo nkukhala Zipatso Zoyamba za iwo amene anagona, ndipo anatumiza Mzimu Woyera ngati chisindikizo cha lonjezo, pa ife, kuti nafenso tidzakhala moyo. “Chifukwa ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo!” Kuwona Kukhalapo Kwake kwakukulu pakati pathu, kukugwira ntchito, kumachita zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa zimene Iye anazichita pa dziko lapansi, kutipatsa ife ziyembekezo. Ndipo ife tabwera ku chiukitsiro, ndiyeno nkumakhalabe pa milu yathu ya phulusa? Tiyeni tichoke pa mulu wa phulusa lero, ndi masomphenya atsopano, ndi Mphamvu yatsopano, ndi kutsimikizika kwatsopano kuti tikumuwona Mulungu mu Mphamvu Yake. Ife tikuwona chiukitsiro cha zinthu ziri nkudza.

64 Ife tiri pa nthawi ya imfa. Ife tikukhala mu zitseko za imfa. Mafuko ali pa zitseko za imfa.

65 Russia wapeza chida chatsopano tsopano, monga inu nonse munamvera pa wailesi ndi chinthu. Iwo sakusowa kuchita kubwera kuno ndi kudzaliphulitsa ilo ndi bomba. Iwo akhoza kungobweretsa kenakake kakang'ono kuno, ndi kudzafika pakati pa azondi awo, ndi kudzalavulira kanthu kakang'ono mu fuko lirilonse, ndipo aliyense akhoza kupuwala kwa maora twente-foro. Kubwera ndipo, pamene iwe ukudzuka, kudzapeza kuti pali wa chi Russia akukumenya iwe mmbali, mlonda wamkulu wa chi Russia akulanda nyumba yako, akumugona mkazi wako, akuwaponyera ana ako panja mu msewu, ndi kumalanda nyumba yako. Iwo akhoza kuchita zimenezo. Iwo sangataye chinthu chimodzi. Iwo ali nazo izo. Palibe amene akudziwa kuti chiyani. Mwaona, chirichonse chikugwira ntchito mmenemo. Tsopano iwo akhoza kugwiritsa ntchito icho ndipo osawopa izo, chifukwa palibe aliyense amene ali nacho.

66 Ife sitikudziwa mmene izo ziti zidzakhalire, zimene ziti zidzachitike. Koma ife tikudziwa chinthu chimodzi, kuti tiri pa mulu wa phulusa. Fukoli, liri pa mulu wa phulusa. Dziko liri pa mulu wa phulusa.

67 Ndipo chifukwa chakuti dziko liri pa mulu wa phulusa, ndine wokondwa kwambiri kuti Mzimu wa Mulungu ukhoza kubwera, ndipo ife tikhoza kunena kuti, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo, ndipo pa tsiku lotsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi ili!” Tsiku lina Iye adzabwera! Nzosadabwitsa wandakatulo analemba:

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine. Pakufa,  
Iye anandipulumutsa ine.  
Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo  
anga kutali.  
Powuka, Iye anandilungamitsa kwaulere  
kwanthawizonse.  
Tsiku lina Iye akubwera, oh, tsiku  
laulemerero!

68 Izo zinatengera Getsemane, madontho a Magazi akutuluka pa khungu Lake, izo zisanachitike. Ndipo izo zinatengera kuzunzika kwa nkhanza kwa Kalvare, pasanabwere chitsimikizo cha Mulungu Wamuyaya Amene akhoza kuwukitsa akufa. Izo zinatengera a—izo zinatengera Getsemane ndi Kalvare, kuti zipange Isitara. Izo ndithudi zinatero.

69 Mmene atumwi amenewo, mmawa umenewo, pamene iwo anali atakhumudwitsidwa kwambiri, mpaka Petro anati, “Ine ndakhumudwitsidwa kwambiri, ine ndikukhulupirira kuti ndingobwereranso kowedza. Ine ndibwereranso kumeneko. Ine, ine ndamuwona Iye.”

<sup>70</sup> Iwo anali ndi ziyembekezo zazikulu, ndipo anakhulupirira ndi chirichonse, mpaka malo aakulu a ndimawo anabwera. Mulungu anali akuchita chiyani? Iye anali akuwabweretsa atumwi amenewo pa mulu wa phulusa. Iye anali kuwabweretsa iwo pa malo amene iwo akanakhala ndi chikhulupiriro chawo chikutsimikizika kwa iwo.

<sup>71</sup> Ndipo Petro anati, “Ine—ine ndinamuwona Iye akuchita zozizwitsa zazikulu uko ku Galileya. Koma, oh, Iye wagona uko, wafa, ndipo wasisima, mmanda! Ine ndikukhulupirira ine ndingotsikira ku nyanja mmawawu ndi kukaponya nkhoka, ndipo ndingopita kumakawedza. Mwinamwake ine ndikhoza kukayang’ana kutsidya kwa nyanja uko, ndipo ine ndikafufuza. Ine ndikukumbukira ndinamuwona Iye pamene Iye ankatidikirira ife pa gombe. Ine ndikukhulupirira ndingotsikira kumeneko.”

<sup>72</sup> Ndipo atumwiwo anati, “Iwe ukudziwa chiyani? Ine ndikukhulupirira ine ndingopita ndi iwe.” Oh, iwo anali okhumudwa. Iwo analira mpaka maso awo kutupa.

<sup>73</sup> Mmene ife timadziwira kudutsa malo amenewo! Mmene ife timadziwira! Ife tonse tinazolowera zinthu zimenezo.

<sup>74</sup> Ine ndikukumbukira pamene ine ndinamuika wokoneddwayo uko mmanda, pamwamba pa chitunda uko, chotchedwa Eastern, kapena Walnut Ridge Cemetery. Mmene ine ndinaikira khanda kumeneko! Ndipo ine ndinkalira mmanja mwa amayi, kufikira, ndinalira mpaka sindikanaliranso. Ine ndinali nditachita chirichonse chimene ine ndinkachidziwa. Mpaka, ine ndinatenga mfuti, kuti ndiyesere kudzipha ndekha, ndinali mu nthawi yoteroyo. Ndipo zinali pa ora limenelo, mu chipinda chaching’ono icho uko, pa maondo anga, pamene Miyamba inatsegukanso, ndipo ine ndinamuwona iye ataima pamenepo mu kukongola kwa chisavundi. Zinali mu ora limenelo pamene ine ndinamverera manja ake atabwera pa mapewa anga, anati, “Bill, iwe sukumvetsa. Ife tiri bwinoko kwambiri kuposa iwe.”

<sup>75</sup> Mwaona, izo zimatengera kupachikidwa. Izo zimatengera kufinyidwa kwa duwa, kuti mafuta onunkhira atuluke kuchokera mmenemo. Zimatengera kufinyidwa kwa moyo, kuti upeze chopambana kuchokera mmenemo chimene chirimo. Nchifukwa chake Yesu ankayenera afinyidwe, kuti atulutse chimene Iye anali. Iye sakanaima kupachikidwa kusanachitike, nkuti, “Mphamvu zonse Mmiyamba ndi dziko lapansi zaparekedwa mdzanja Langa.” Koma pambuyo pa kupachikidwa, Iye anatha kuima ndikuti, “Mphamvu zonse Mmiyamba ndi dziko lapansi zaparekedwa mdzanja Langa!” Koma kodi izo zinachita chiyani? Zinatengera kupachikidwa poyamba.

<sup>76</sup> Izo zinatengera kufinyidwa ndi kukhumudwitsidwa kwa atumwi. Iwo anali atamuwona Mpulumutsi wawo, Iye amene iwo ankamukonda, ndipo anamuwona Iye akuukitsa ngakhale akufa kwa—kuchokera mmanda. Iwo anali atamuwona Iye akuchita zimenezo. Ndipo kenako nkuganiza, “Uko Iye wagona, wasisima, mmanda, Iyemwini, mmawa uno.” Izo zinatengera a . . .

<sup>77</sup> Anthu awo amene anali atamuwona Iye akutsegula maso a akhungu, anamuwona Iye ataima pamenepo ndi kuzindikira malingaliro kumene amene anali mmitima ya anthu, “Iye wadziwa bwanji,” iwo amakhoza kunena, “kuti iwo akumufuna Iye? Iye wadziwa bwanji? Nchifukwa chiyani Iye sanamuziwe Yudasi, Yudasi akanadza—akanadzamupereka Iye? Nchifukwa chiyani Iye sanadziwe kuti asirikali ankabwera kumtunda pa phiri pamenepo, ali ndi ndodo ndi malupanga ndi chirichonse, kuti adzamugwire Iye, ngati Iye amatha kuzindikira malingaliro awo?”

<sup>78</sup> Mwaona, mdierekezi anali akugwira ntchito pa iwo, kuwayika iwo pa mulu wa phulusa, chifukwa iwo ankafuna kuwapatsa iwo umboni wa “Ine ndikudziwa.” (Osati “Ine ndikuganiza” kapena “mwinamwake ziri chomwecho.”) “Ine ndikudziwa! Ine ndikudziwa!”

<sup>79</sup> Ndipo kumbukirani, mayesero amenewo amabweretsedwa pa inu mwanjira yofanana, kuti inu musanene kuti, “Chabwino, mwinamwake Ichi ndi choona, mwinamwake Lemba ndi lowona, mwinamwake machiritso Auzimu ndi owona, mwinamwake Mzimu Woyera ndi woona.” Koma pamene inu mukhala ndi chokuchitikirani chimenecho ndi kuchokapo pa mulu wa phulusa uwo, ndipo nkupeza vumbulutso la Mulungu, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, inu mukhoza kufuula, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo, chifukwa Iye akukhala mwa ine!”

<sup>80</sup> Petro anati, “Ine ndipita ndizikawedza.” Atumwi anati, “Ine ndikukhulupirira ndingopita ndi iwe.” Ndipo apo iwo anali pa mulu wawo wa phulusa, kumusi uko pakati pa nyanja, ndipo mavuto akuchitika mmene zinkakhalira. Ndipo ine ndikukhoza kumumva mmodzi wa iwo akuti, “Oh, zatheka bwanji, Petro? Zatheka bwanji kuti Munthu ngati ameneyo afe? Zingatheke bwanji kuti Iye waikidwa mmanda mmene Iye wachitiramu? Zinatheka bwanji kuti Iye analolera kuti iwo amulavulire pa nkhope Yake ndi kumumwetula ndevu, ndi kumuveka chisoti chija pa mutu Pake? Iye anatha bwanji kuchita zimenezo, oh, ndipo nkukhalabe Mulungu? Ine basi ndikulephera kumvetisa zimenezo.” Oh, ndi zokhumudwitsa bwanji!

<sup>81</sup> Ndipo mwadzidzidzi, iwo anayang’ana pagombe, basi mtundu womwewo wa vumbulutso limene Yobu anali nalo, pamenepo iwo anawona chimene Yobu anachiwona zaka foro sauzande mmbuyo. Pamenepo panaima Muomboli, wamoyo



ndi watsopano, atayima pa gombe. Atasonkha moto, ndipo nsomba zikuphikidwa pamenepo monga choncho, ndipo anati, anawaitanira iwo.

Yesu wakonza gome  
 Pomwe oyera a Mulungu akudyapo,  
 Ayitana osankhidwa Ake “Dzadyeni;”  
 Ndi manna Ake Iye awadyetsa  
 Chosowa awapatsa;  
 Oh, izo, nzokoma kudya ndi Yesu nthawi zonse!

Mmene ife tingaganizire zimenezo, mmene zinatengera zinthu zapamwamba izo!

<sup>82</sup> Mmene kuti a...Paulo mtumwi, mtumwi wamkulu uja amene anakadutsa mu nthawi yake ya mavuto pamene anachitira umboni imfa ya Stefano; ndipo anawona nkhope yake yaing’ono ikuyang’ana Kumwamba, ndipo miyala ikumugenda iye pa nkhope, ndipo iye anayang’ana mmwamba ndipo anati, “Ine ndikuwona Miyamba itatseguka. Ine ndikumuwona Yesu waima pa dzanja lamanja la Mulungu.” Iye anati, “Ambuye, musayike tchimo ili pa iwo.” Ndipo Paulo atanyamula zikhoti, zimene zinamuyika iye kwa masabata pambuyo pa masabata pa mulu wa phulusa, akungoyendayenda; mpaka, malingaliro ake anasokonezedwa, mpaka iye anali panjira yake waku Damasiko, kuti akayesere kumenyana nazo, monga munthu kupita ku botolo la mowa, kuyesetsa kuti atontholetse chisoni chake.

<sup>83</sup> Iye anali mkati mwa zimenezo, pamene panadzabwera Liwu kuchokera Kumwamba, Kuwala kwakukulu kunati, “Saulo, Saulo, nchifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?” Iye anamuwona Iye. Iye anamuzindikira Iye, kuti Iye anali Yesu woukitsidwa, Iye amene anamuwona akufa, anawukitsidwanso.

<sup>84</sup> Oh, ine ndikukhoza kukumbukira moyo wanga womwe, pa njira waku chiwonongeko, pamene ndinamva Liwu lokoma, “Ine ndine Yesu. Ine ndinali wakufa, ndiri wamoyo kwa nthawizonse. Chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mukhoza kukhala moyo.” Kuyambira nthawi imeneyo, kuyika dzanja langa mu Lake, ine ndamudalira Iye kudutsa mmalo a mdima. Pamene nthawi zifika pamene ine sindingathe kuwona, njira imene ndikupita, ine ndidzamudalirabe Iye.

<sup>85</sup> Mkhristu wokhulupirira aliyense akuyenera kukankhidwira mu mayesero amenewo. Mkhristu wokhulupirira aliyense akuyenera kuyikidwa pa mulu wa phulusa, kuti atulukeko ndi chomuchitikira, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo!”

<sup>86</sup> Ife sitinabwere kuno mmawa uno kudzangokhala ndi kudzayankhula za zochitika zakale zina, zimene zonse ndi zoonza, koma ife tabwera kuno ndi umboni mmawa uno, “Ine ndikudziwa kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, ine ndikudziwa izo kudutsa mthunzi wa kukaikira uliwonse! Ine ndikudziwa kuti Iye anauka kwa akufa, ndipo Iye akukhala

moyo mwa ine lero. Iye ndi wanga ndipo ine ndi Wake. Ine ndi wolowa limodzi ndi Iye, mu Ufumu wa Mulungu.”

<sup>87</sup> Isitara! Isitara imabweretsa chinthu chachikulu, chiukitsiro, chiyembekezo chatsopano. Kodi inu muli nacho icho mmawa uno? Kodi icho chiri mu mtima mwanu? Kodi inu mukudziwa kuti Muomboli wanu ali moyo, ndipo Iye akupangitsa zinthu zonse kumagwira ntchito limodzi?

<sup>88</sup> Inu mukuti, “M’bale Branham, ine ndakhala pano, ndikudikirira mzere wa pemphero.”

<sup>89</sup> Mulungu akuchita zimenezo ndendende kwa ubwino. Nchifukwa chiyani mnyamata wofunika uja, tsiku lina, anabadwa wakhungu? Kuti Mulungu apeze ulemelero ndi kutembenuza mzindawo chadodolido. Ndithudi, Mulungu amadziwa chimene Iye akuchita. Mulungu amadziwa. Ndipo Iye amatiika ife pa mulu wa phulusa, ndi cholinga chakuti atiwonetse ife ulemelero Wake.

<sup>90</sup> Chotero, mmawa uno ine ndikunena izi, mzanga. Patadutsa zaka sarte-wani za utumiki, patadutsa zaka sarte-wani za kuvutika mmunda, ine ndikufuna ndipange umboni wanga kwa izi. Ine ndawonapo zokhumudwitsa. Ine ndawonapo nthawi zimene ine ndinapemphapo zinthu, ndi kulirira zinthu, ndi kupempha zinthu, ndipo nkulephera kuti ndizipeze izo. Koma ngati ine ndingodikirira mwachipiriro pa Mulungu, ndiye ine ndikudziwa kuti izo zimagwira ntchito ndendende basi, zimabwera ndendende basi, zimachita ndendende basi chinthu cholondola.

<sup>91</sup> Pamene ine ndinataya mwana wanga, Sharon wanga wamng’ono, ine...chimenecho chinali chinthu chimodzi chimene chinandipunthwitsa ine. Ine ndinati, “Izo zingakhale bwanji kwa ubwino? Izo zingakhale bwanji kwa ubwino?” Ndipo miyezi mtsogolo, pamene ine ndinadzamuwona iye atayima pamenepo mu kukongola konse kwa mtsikana wachichepere, akundiyankhula ine, nditaima pambali pa ngolo yakale yowonongeka iyo, pamenepo. Ine ndinadziwa, ngati iye akanakhala moyo, iye mwina akanalakwa. Mulungu amayenera kumutenga iye pamene iye anali wamng’ono ndi wokoma. Ine ndikudziwa ndidzamuwonanso iye. Ine ndikudziwa ndidzamuona iye, ine ndikudziwa izo mopanda mthunzi uliwonse wa kukaikira.

<sup>92</sup> Ine ndimaganiza za mkazi wanga wa usinkhu wa zaka twente-thuu zakubadwa, atatengedwa, ali mtsikana basi, mayi wamng’ono pamenepo. Pamene mapepala analemba mutu wa nkhani apa, “Mayi wamng’ono, abusa... akufa kumene,” oh, mmene mtima wanga unakhetsera magari! Ine sindinadziwe choti ndichite.

<sup>93</sup> Koma lero ine ndikudziwa izo zonse zinkandichitira ine ubwino. Ine ndikudziwa moyo umayenera kuphwanyidwa,

ndi kuvuvunyidwa, ndi kufinyidwa, kuti utulutse zimene zinali mmenemo, powonekera. Munali Branham wochuluka kwambiri mmenemo, amayenera kuti afinyidwire panja Mulungu asanazizindikiritse Yekha.

<sup>94</sup> Munali inu wochuluka kwambiri mwa inu, mpaka Mulungu anachita kumufinyira iye panja, kudzera mu mayesero. Ndipo pamene kufinya kumeneko kumabwera, izo zimakhala zovuta. Koma patapita kanthawi, miyamba imakanganuka, kenako inu mumawona cholinga cha Mulungu. Kenako inu mumafuula, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo, ndipo mmasiku otsiriza Iye adzayima pa dziko lapansi! Ngakhale mphutsi za mkhungu zitawononga thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzawonona Mulungu!” Mayesero aang’ono awa ndi zinthu ndi za kanthawi chabe, ndipo izo zimazimirira ndi kuchokapo. Koma izo zimangochitika kwa ubwino wanu, tiyeni ife tizikumbukira zimenezo, kuti Mulungu apezze ulemelero.

<sup>95</sup> Tiweramitse mitu yathu kwa mphindi chabe. Ine ndikufuna ndifunse, tisanapemphere, kodi alipo aliyense pano amene akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero ife tisanatseke? Mulungu akudalitseni inu. Ndi angati muno angati, “Ine ndikumufuna Mulungu, mu ora la mayesero anga tsopano, kuti andipatse ine chondichitikira chatsopano, kuti ine ndibwere watsopano kenanso?” Kwezani dzanja lanu, ndikuti, “Ine ndikufuna—ndikufuna ichi chikhale chiukitsiro changa, Isitara, kuti indiwukitse ine mu ziyembekezo zatsopano ndi mphamvu zatsopano, thanzi latsopano ndi chimwemwe chatsopano.” Ambuye akudalitseni inu, anthu anga okondedwa.

<sup>96</sup> Oh, Mulungu wathu ndi Mpulumutsi wathu, ife ndi othokoza kwambiri kwa Inu chifukwa cha Isitara iyi, chifukwa cha chimene iyo ikutanthauza ku mitima yathu. Ndipo mwa chikhulupiriro, kutsidya uko, kudutsa dzikolo, ife tikukhoza kuwona Kudza kwa Ambuye, Yesu, pamene Iye akudzikonzeke retsa Yekha tsopano, akuvala zovala Zake zachifumu. Ndipo, Mpingo ukuvala, Mkwati akuvala chovala Chake cha chikwati. Pakukonzekera kudzakhala msonkhano waukulu posachedwapa.

<sup>97</sup> Mulu wa phulusa uwu sungakhalepo kwa nthawizonse. Pamene ife tikumva anthu akuseka, akutisereula ife, ndi kumatitcha ife dzina lonyoza la “oyera ozigudubuza,” ndi kumatisereula ife, ndi kumanena kuti ife sitiri olongosoka nkomwe mmalingaliro, oh, izo sizingakhale nthawi zonse, Ambuye. Koma mutilole ife tikhale monga Yobu, tigwire umboni wathu, mutilole ife tikhale monga Daniele mu dzenje la mikango, kapena ana Achihebri pa ng’anjo yamoto, kapena Abrahamu pa ulendo wake.

<sup>98</sup> Tithandizeni ife, O Ambuye, kuti tiime owona mpaka tidzawone chinthu chachikulu icho chikuchitika, “Pamene

lipenga lidzalira, ndipo akufa mwa Khristu adzauka; ife amene tiri moyofe ndipo tatsalira tidzasinthidwa, mu kamphindi, mu kuthwanima kwa, diso.” Ndipo kenako padzabwera Isitara imeneyo kwa ife, imene Khristu anasangalala nayo zaka naintini handirede zapitazo mmawa uno, ndipo anati, “Chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo.”

<sup>99</sup> “Yesu yemweyu, amene anatengedwera mmwamba kuchoka pakati pathu, adzabwereranso basi mmene Iye anapitira.” Ife tidzamuwona Iye, ngakhale chipsyera chirichonse mu dzanja Lake ndi chidindo cha minga chirichonse pa mutu Wake. Ife tidzamuwona Iye.

Oh, ndidzamudziwa Iye, ndidzamudziwa Iye,  
Ndipo woomboledwa pambali Yake ine  
ndidzaima.

<sup>100</sup> Inde, Ambuye, mtima wanga wosauka, pamene thupi lofooka langali likuyamba kuwerama ndi mtolo, nkhwana ndi zosautsa za mminda yokolola, minda ya umishonare, ndi zokwera ndi zotsika, ndi kusayanjanitsika pakati pa atumiki amwano, ndi zina zotero, kudutsa pa malowa, ndipo anthu akunyozza, ndi mphamvu zoyipa. Koma, O Ambuye, tsikulina ife tidzabwera monga Eliya, kutsika kupita ku mtsinje; kuyang’ana kumeneko, atamangiriridwa ku tchire lirilonse, galeta la moto limene lidzatitengere ife kutali. Tiloleni ife tidziwe kuti milu ya phulusa iyi ndi zophimba chabe zoti zitibise ife kwa chinthu chachikulucho chimene chiri patsogolo, ulemelero waukulu uwo.

<sup>101</sup> Mulole ife tikhale owona monga Yobu, mpaka ife tidzamuwone Iye, maso ndi maso. Mulole ife tikhale owona mmene Ambuye wathu anachitira, ngati chitsanzo chathu, tikupita ku Kalvare; nafenso, okonzekera kuti tipachikidwe, ndi kupachikidwa ndi Iye, kuti padzakhoze kukhala chiukitsiro mmooyo mwathu. Perekani izi, Ambuye.

<sup>102</sup> Mulole, ngati pangakhale onyoza aliyense pano, amene anali monga Paulo wakale, amene wasereula, mulole iwo akaipeze Isitara pa njira yawo akamapita kwawo mmawa uno. Perekani izi, Ambuye.

<sup>103</sup> Ife tikupemphera, Ambuye, kuti iwo amene ali pa mulu wa phulusa wa chiwonongeko, mulu wa phulusa wa matenda, kuti ili likhale ora limene iwo ati adzapulumutsidwe.

<sup>104</sup> Usiku wathawu, ndikuyankhula ndi mkazi wamng’ono uja uko pa ngolo, ndi mwamuna wake; mmene uko mu Phoenix, mu chochitika chovuta, ndipo ma khansa aakulu awo ali pamenepo pa iwo, ndipo tsofano lero ali bwinobwino mwangwirowo ndipo amphumphu. Ndi mwana wamng’ono amene anali woti mtima wake uchotsedwa, wakhala apa mchipinda chino mmawa uno, wamphumphu, ali bwino. Mnyamata wamng’ono wakhungu amene anayendapo mu mdima ndipo sanawonepo kuwala kwa

tsiku, akuyenda lero ndipo akuwona kuwala kwa tsikuli. Ndipo, O, Mulungu, mmene ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha ichi! Ndipo izo zonse zikuyang'ana kudutsa chophimba, kupita ku tsiku lalikulu limenelo la chiukitsiro. Perekani izi, Atate. Ndipo mulole iwo adziwe kuti zinthu izi zinkayenera kukhala mwanjira imeneyo, kuti awa: mnyamata wamng'ono wakhungu athe kuwona, kuti mwana amene ali ndi vuto la mtima athe kupereka umboni kwa ena. Zinthu zonsezi zimagwira ntchito pamodzi kwa ubwino wa iwo amene amakukondani Inu.

<sup>105</sup> Zonse zimatheka kwa ife chifukwa panali Mmodzi wodzichepetsa mu yesero, analipo Mmodzi Amene anayima ndi yesero, ameneyo anali Yesu. Iye Uyo Amene anali womvera kwa Atate, mpaka Atate anamuukitsa Iye mmawa wa Isitara, chifukwa izo zinali zosatheka kuti Iye agwidwe ndi imfa. “Pakuti Ine sindidzalola Woyera Wanga Uyo awone chivundi, komanso sindidzasiya solo Yake mu gehena.” Pakuti, Iye anapezeka wokhulupirika, nthawizonse akuchita icho chimene chimawasangalatsa Atate.


<sup>106</sup> Mulungu, mulole ife nthawizonse tizikhala okhulupirika pa malo antchito. Ziribe kanthu kuti mayesero athu ali chiyani ndi mavuto athu, chirichonsecho, mulole ife tidzakwanitse kunena, nthawizonse, “Ine ndikudziwa kuti zinthu zonse zimagwira ntchito limodzi kwa ubwino wa iwo amene amamukonda Mulungu.” Perekani izi, Atate.

<sup>107</sup> Ife tikuwadalitsa anthu awa mmawa uno ndi madalitso Anu. Iwo abwera molawirira kuchokera ku malo awo, iwo abwera ku kachisi. Iwo abwera kuti adzapeze chitonthozo. Mulole iwo apite kwawo mmawa uno, ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera ukuyaka mmitima yawo, akuyendayenda pa njira monga iwo ankachokera ku Emawu, akuti, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula nafe pa njira?” Perekani izi, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Amen.

Chabwino, M'bale Neville. Ndipo tsopano mukumbukire misonkhano.

<sup>108</sup> Ife sitikhala ndi makadi apemphero mmawa uno, chifukwa chakuti, ife tikakhala ndi makadi apemphero, pamene ine ndiwaimiritsa anthu amenewo pano monga choncho, ine ndizidalira mphatso imeneyo. Ine ndikuyenera kukhala ndi malo amene ndingazisiye izo pambali, pamene ine ndikhoza kumayenda kuno ndi kukhoza...ine ndikuwopa. Ine ndikuwoneka kuti ndikuchita mantha, ndipo ndikuwopa kuti ndilakwitsa. Kugonja ndewu, si kugonja nkhondo. Patton anagonja ndewu zingapo, koma sanagonje nkhondo. Uko nkulondola. Ndipo ife tizigonja ndewu zochuluka, nafenso, koma sitidzagonja nkhondo. Ine ndizipanga zolakwitsa zambiri, koma sindidzagonja Cholingacho. Mulungu anapereka izo,

ndipo Mulungu adzasamalira izo. Ndizo—ndizo kuzodza. Ndipo tsopano ndi nthawi, ine ndikukhulupirira kuti oralo ndi pano, ndipo ine ndikuyamba, pokhala kuti ndi Isitara lero, Ine ndizipita—ndizipita nawo monga ine ndinachitira pamenepo ndikupempherera odwala. Ndipo ngati ine ndingathe... Ndi kuzodza. Ndi chinachake chimene chikuyenera kuchitika mkati mwanga. Ine sindinachizolowere icho. Icho chimabwera mwanjira yakuti, ine mwina sindingakwanitse kuzindikira icho molondola, koma ine ndikuyenera kumapitabe kwa icho mpaka nditadziwa icho nthawi iliyonse. Chotero ili likhala tsiku limene ine nditayesere, mwa chisomo cha Mulungu.

<sup>109</sup> Ambuye akudalitseni inu tsopano. M'bale Neville. Ndipo misonkhano iyamba hafu pasti-naini. M'bale Neville. 

*INE NDIKUDZIWA* CHA60-0417s  
(I Know)

MAULALIKI A ISITARA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi pa Lamlungu la Isitara pa kutuluka kwa dzuwa, April 17, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)